# UNDUNA WA ZA CHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA CHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA, M'DZINJA LA 2025-2026 M'BOMA LA DEDZA

## Nyengo yadzinja ya 2025-2026 Mwachidule

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/2026


Boma la Dedza likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena mlingo woposera wokhazikika mu nyengo ya mvula ya 2025/2026

## October 2025




Mwenzi wa October ukuyembekezeka kuzakhala wopanda mvula m'madera ambiri. Komabe mvula ya Chizimalupya ikuyembekezereka mumadera ochepa yamulingo osaposera 10mm. Mvulayi ikhoza kuzabwera ndi mabingu komanso mphepo ya mkutho.


## November 2025




Madera ambiri akuyembekezera kuzalandira mvula ya mulingo wapafupifupi 50 mm yomwe ndi mvula yochepera mulingo wokhazikika.

Mphepo ya mkutho komanso mphezi zikuyembekezereka mu mweziwu.


## December 2025




Mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposerapo ikuyembekezereka mu madera ambiri, ndipo madera ena a kwa T/A Pemba komanso Kaphuka akuyembekezereka kulandira mvula ya mulingo wa 300 mm

Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kuyamba sabata lachitatu la mwezi wa December.

## January 2026





Mvula ya mulingo wokhazikika kapena kuposerapo, yoyambira 250 mm kufika 300 mm, ikuyembekezereka m'madera ambiri.

Komabe madera ena ochepa a kwa T/A Pemba komanso a kwa T/A Kaphuka akuyembekezereka kulandira mvula yosaposera 200 mm yomwe ili yochepera mulingo wokhazikika.

Ng'amba yapafupifupi sabata limodzi likuyembekezereka mu mweziwu.

Longitude

## February 2026





Mvula ya mulingo wokhazikika kapena kuposerapo, ya mulingo wa wapakati pa 250 kufikira 300 mm, ikuyembekezereka m'madera ambiri

Komabe madera ochepa a kwa T/A Pemba ndi T/A Kaphuka ikuyembekezereka kulandira mvula ya yapafupifupi 200 mm yomwe ndi mvula yochepera mulingo wokhazikika.


Ng'amba ya masabata awiri ikuyembekezerekanso m'mweziwu.

## March 2026




Madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvula yapafupifupi 200 mm yomwe ndi mvula yoposerapo mulingo wokhazikika

## April 2026




Mvula yapakati pa 50 mm and 100 mm yomwe ndi mvula ya mulingo wokhazikika kapena kuposera apo ikuyembekezereka.


Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto mu sabata lachitatu la mwezi wa April.

Mu boma la Dedza, mvula yodzalira ikuyembekezereka kuyamba pakati pa mwenzi wa December,2025, ndipo nyengo ya dzinjali ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata yachitatu mwenzi wa April, 2026.

Pali kuthekera kokhala ng'amba ya sabata imodzi mu January, ndi ng'amba yasabata ziwiri mu mwenzi wa February. Nyengo ya dzinjali ikuyembekezereka kukhala ya masiku oyambira 120 kufikira 130.

The table and figure below show monthly rainfall distribution for the season with a normal band in grey.

| DEDZA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 1.114 | 12.06 | 9.6 |
| NOV | 29.628 | 76.676 | 42.5 |
| DEC | 143.539 | 221.331 | 210 |
| JAN | 205.435 | 277.798 | 278.5 |
| FEB | 174.543 | 259.82 | 185.4 |
| MAR | 108.181 | 171.381 | 174.1 |
| APR | 18.557 | 54.497 | 69.7 |




**The forecast will be updated in December 2025**

For further information contact: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Produced and printed with support from: